Kuuzindikira Mzimu

Atate athu Akumwamba, ine ndikufuna kuti ndifotokoze, ngati ine ndingakhoze, mmawa uno, momwe mu mtima mwanga ine ndikumverera kwa Mmodzi, Woyeretsetsa pa Oyera, kubwera pansi ku dziko lapansi, ndi kudzawombola wochimwa monga inemwini. Ndipo ine ndikutsimikiza kuti atumiki awa omwe alipo tsopano, akhoza kumverera mwanjira yomweyo, kuti zinali mwa chisomo Chanu kuti ife tapangidwa kukhala atumiki a pangano ili, limene Inu mwalipereka ndi mtundu wakugwa wa Adamu. Ndipo ife tiri pano mmawa uno, Atate, osonkhana osati kwa cholinga china koma kuti tidziwe, ndi kuphunzira ku—kuti tidziwe, kani, chifuniro cha Mulungu ndi chimene ife tiyenera kuchichita kuti timupange Khristu kukhala weniweni kwa anthu a m'badwo uno. Podziwa motsimikiza kuti mu tsiku la Chiweruzo, ife tidzabweretsedwa maso ndi maso ndi m'badwo uno. Ndipo, pokhala atumiki, ife tidzakhala tiri oweruza. Ndi anthu omwe ife tayankhula nawo, ndi cholinga chawo kwa Mawu omwe ife tikuwabweretsera iwo, zidzatsimikizira kopita kwawo Kwamuyaya. Chotero, Ambuye, mu tsiku limenelo ife tidzakhala woweruza kapena otsutsa m'badwo umene ife tinalalikira kwa iwo.

2 Atate, Mulungu, chonde, kupyolera mu Dzina la Yesu, musatilole ife tinene mawu amodzi amene akanati akhale olakwika. Koma mutalola ife tikhale ndi mitima yodzipereka ndi malingaliro otseguka kuti ife tikhoze kumalandira zinthu zomwe ziri Zanu, kuti ife tikhoze kupita kunja mu malo athu osiyana antchito, likatha lero, ndi—ndi kukakhala nazo zida mwabwino chifukwa cha kusonkhana kwathu ndi Inu mmawa uno. Perekani izi, Ambuye. Kodi Inu simubwera ndi kudzakhala wotiyankhulira wathu ndi makutu athu, ndi lirime lathu ndi maganizo athu? Mulole kusinkhasinkha kwa mtima wanga, maganizo a malingaliro anga, zonse zomwe ziri mkati mwa ine, ndi mkati mwa abale anga awa ndi alongo, mulole izo zikhale zolandiridwa pamaso Panu, Ambuye, kuti ife tikhoze kukhala odzazidwa kwambiri ndi opatsidwa nyese ndi Mzimu Wanu, wa Kukhalapo Kwanu pano, kuti chipinda chikanakhala . . . chipinda, osati mochuluka kwambiri nyumba yomwe ife takhalamo, koma nyumba yomwe ife tiri kukhalamo, ikhale palimodzi mtambo wa Ulemerero wa Mulungu. Ife tikhoze kuchoka pano mmawa uno odzazidwa kwambiri ndi Mzimu Woyera kuti ife tikakhoze kukhala otsimikiza mochuluka kuposa kale lonse mu moyo kuti tikatengere Uthenga kwa m'badwo wokufa womwe ife tiri kukhalamo. Timveni ife, Ambuye, ndipo muyankhule kwa ife kupyolera mu Mawu anu, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Mwana Wanu ndi Mpulumutsi

wathu, Yesu Khristu. Ameni.

3 Ine ndikufuna kuti ndiwerenge, mmawa uno, g—gawo la Lemba lopezeka mu Masalmo, Salmo la 105. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge kagawo kokha. Inu amene mumasunga kuwerenga kwa Malemba uku; ine ndikuwona ochuluka a iwo; ndipo pokhala kuti ndife atumiki ndi ena otero. Ndi zabwino kuti tiwerenge Mawu. (Ndipo, tsopano, kodi ndi nthawi yanji yomwe iwo amakonda kuchoka, pafupi thwelofu koloko? Mukuti chiani? Zikomo inu.) Masalmo 105:

O perekani mayamiko kwa YEHOVA, itanirani pa dzina lake: dziwitsani zochita zake pakati pa anthu.

Imbirani kwa iye, imbani masalmo kwa iye: yankhulani inu za ntchito zake zonse zodabwitsa.

Mudzitamandire inu mu dzina lake lopatulika: mulole mitima *ya iwo ikondwere omwe amfunafuna YEHOVA.*

Mfunefuneni YEHOVA, ndi mphamvu zake: funafunani nkhope yake mochulukirabe.

Kumbukirani ntchito zake zododometsa zomwe iye wa*zichita; zodabwitsa zake, ndi ziweruzo za kamwa yake;*

O inu mbewu ya Abrahamu antchito *ake,* ndi *inu ana a Yakobo osankhidwa ake.*

Iye ndi YEHOVA Mulungu wathu: ziweruzo zake ziri mu dziko lonse lapansi.

Iye wa*kumbukira pangano lake kwanthawizonse*, mawu *omwe iye anawalamulira kwa mibadwo zikwi.*

Pangano lomwe iye analipanga ndi Abrahamu, ndi lumbiriro lake kwa Isaki;

Ndipo anatsimikizira lomwelo kwa Yakobo likhale lamulo, ndi kwa Israeli likhale pangano losatha:

Kuti, Kwa iwe ine ndidzakupatsa dziko la Kanani, gawo la cholowa chako:

Pamene iwo anali koma anthu *pang'ono mu chiwerengero; eya, apang'ono kwambiri, ndi alendo mmenemo.*

Pamene iwo anapita kuchokera ku fuko limodzi kupita ku lina, ndi *kuchokera ku ufumu wina kupita kwa anthu ena;*

Iye sanalole munthu aliyense kuti awachitire iwo cholakwika: eya, iye anadzudzula mafumu chifukwa *cha iwo*;

Nati, Musamawakhudze odzozedwa anga, *ndipo musamawachitire aneneri anga chowapweteka.*

4 Ambuye atadalitsa kuwerenga kwa Mawu Ake. Ine ndiri ndi Malemba pang'ono ndawalemba pano penapake omwe ine ndimati ndilozereko mwina popita mnjirayi.

5 Ine ndikudabwa, lero, ndi ndani ati akhale Purezidenti wotsatira? Zisankho zikubwera, inu mukudziwa. Ndi ndani ati akhale Purezidenti nthawi yotsatira iyi? Bwanji ngati ine ndikanadziwa? Alipo mmodzi yekha yemwe akudziwa, ndipo ameneyo ndi Mulungu. Ndipo nanga bwanji ngati Mulungu akanati aululire kwa ine yemwe akanati akhale Purezidenti wotsatira, ndipo ine ndikanaima pano mu Phoenix ndi kupanga kuneneratu kuti munthu wakuti-n-wakuti akanakhala Purezidenti wotsatira wa United States? Ndipo iwo akanazilemba izo mu mapepala ndi zina zotero, ndipo ine ndikanakhala nditazigunda izo pa dontho. Izo zikanakhala ziri zangwiro, ndipo izo zikanakhala kuti zonse zomwe ine ndinanena zomwe zikanafika pochitika. Koma izo zikanati zichitire ubwino wanji? Nzaubwino wanji izo, mulimonse, ngati ine—ngati ine ndikanati ndichite chinthu choterocho? Mapepala akanati alengeze izo, ndipo izo zikanati zipite kunja mwinamwake, ngati munthu ameneyo akanati apange kuneneratu koteroko ndipo izo nkukhala zoona, mapepala onse ndi magazini akanati—akanati alengeze pa izo.

6 Koma inu mukudziwa kuti Mulungu samachita zinthu monga choncho, Mulungu samagwiritsa ntchito mphamvu Zake ndi mphatso Zake kwa zopusa. Iye akhala, Purezidenti aliyense, iye adzakhala Purezidenti. Ndipo kudziwa tsopano yemwe ati akhale Purezidenti, sizikanati zitithandize ife khobidi limodzi. Izo sizikanati zitichitire ife chidutswa chimodzi cha ubwino kudziwa yemwe akanati akhale Purezidenti. Ndiye chotero, Mulungu samachita zinthu zimenezo monga choncho.

7 Ndipo, ndiye, ngati ine ndikanapanga kuneneratu koteroko monga iko, ndipo izo nkudzachitika, ndipo manyuzipepala nkulemba izo, ndi magazini, ndiye izo zikanati zikhale kwa ulemerero wanga. Anthu akanamati, "Taonani mneneri wamkulu yemwe M'bale Branham ali. Iye anatiuza ife kale litali izo zisanachitike basi yemwe akanati adzakhale Purezidenti." Ndipo izo zikanakhala kwa ulemerero wanga. Koma Mulungu safuna . . . Iye sakondweretsedwa nako kuchita zinthu kwa ulemerero wanga, kapena kwa—kwa ulemerero wa munthu wina aliyense. Iye amakondweretsedwa kuchita zinthu kwa ulemerero Wake, chinachake chimene chikanati chipindulitse.

8 Monga Paulo anati, "Ngati ife tiyankhula ndi malirime ndi kusakhala naye wotanthauzira, izo zingachite ubwino wanji? Ife timangodzipatsa tokha ulemerero," ndipo, ndizo, kapena "kudzimangiriza tokha." Ndizo zokhala ngati kuchoka pa mzere wa Mulungu. Mulungu amafuna kuti azimangirizidwa Mwiniyekha. Ndipo ife si oti tizifunafuna kudzimangiriza-

kwatokha, koma kuti tizimumangiriza Mulungu ndi zonse zomwe ife timachita.

9 Ndiye chotero, ine ndikukhulupirira mmawa uno, ngati ine ndikanadziwa yemwe akanati adzakhale ali ndi ndendende pamene iye akanati adzasankhidwe, ndi, o, ndi mavoti angati akanati adzapambanire kapena kuperewera, kapena chirichonse chomwe izo zikanati zikhale ziri, izo sizikanati zichite ubwino wa kugunda kumodzi kuti uzinene izo. Izo zikanakhala zabwino kuti ine ndingozisunga izo mwabata ngati ine ndikanati ndizidziwe izo. Osati kuyesera kuzilengeza izo, chifukwa pakanakhala—sipakanakhala chifukwa choti ine ndichitire izo. Chifukwa, izo zidzakhala ziri, mulimonse, ndipo izo sizimatipangitsa ife kusiyana kochuluka chotero yemwe ati akhale Purezidenti.

10 Koma, Mulungu, pamene Iye agwiritsa ntchito mphatso Zake, Iye amazigwiritsa izo ntchito kwa ulemerero Wake womwe, ndi kwa ulemerero wa anthu Ake, kwa ulemerero wa Mpingo Wake, kwa kumangiriza kwa Thupi la Khristu, ndi kwa ulemerero wa Ufumu wa Mulungu. Ndicho chifukwa Iye amapereka zinthu izi mu Mpingo Wake, chifukwa chomwe Iye ali ndi aphunzitsi, mneneri, avangeri, azibusa. Iwo ali a kumangiriza kwa Mpingo ndi kwa ulemerero wa Mulungu. Mneneri si woti azituluka ndi kumakasakanizana ndi dziko ndi kuyesera kuitenga mphatso monga Balaamu anachitira, ndi kupanga chisokonezo kapena—kapena ndalama kuchokera mu iyo kapena chinachake. Ngati iye ali mneneri, iye akuyenera kuti aziwululira Mulungu kwa Mpingo ndi kukhala kunja kwa zinthu za mdziko. Zonse ndi za kwa ulemerero wa Mulungu!

11 Tsopano ife tiri nazo . . . ndipo ine ndikuganiza ndi chinthu chabwino kwa ife, monga atumiki, kuti tizitsatira dongosolo lathu, pamene ife tiwona zinthu zotero mu dziko monga ife tikuziwona lero. Ndipo ife tiri ndi dongosolo lochokera kwa Mulungu, ndilo la kuzindikira mizimu, kuwuyesa mzimu. Ine ndikukhulupirira kuti ilo ndi phunziro lalikulu kwambiri la kwa mpingo lero, ndiko kuti tiziuyesa mzimu wa chirichonse, kukhala nako kuzindikira kwa mzimu. Ine sindikuganiza kuti ife tiyenera konse, mwa njira iliyonse, kuyesera konse kumuweruza munthu ndi chipembedzo chimene iwo alimo, kapena gulu lomwe iwo amasonkhana nalo, kaya iwo akhala ali Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Apentekoste, kapena—kapena chirichonse chomwe iwo ali. Ife tisamamuweruze konse munthu ndi chipembedzo chomwe iye alimo. Ife nthawizonse tizimuweruza iye ndi mzimu womwe ali nawo, mwaona, mzimu. Kaya iye ndi wa mvula yamasika kapena yanyundo kapena yamkati, mvula yakunja, kapena wopanda mvula, kapena chirichonse chomwe icho chingati chikhale chiri, ife tisamamuweruze konse iye ndi izo, koma, ndi mzimu wake. Ife tiri oti tiziuzindikira mzimu. Kupenya chimene munthu ali

nacho mu malingaliro, chimene iye ali nacho . . . chimene iye akuyesera kuti achikwaniritse. Ngati munthu, ndi mphatso, ziribe kanthu momwe mphatsoyo iliri yayikulu . . .

12 Tsopano ine ndikufuna kuti ndifikitse izi kwa Mpingo mmawa uno, chimene, mu zipembedzo zosiyana inu mukadali Mpingo wa Mulungu wamoyo, palimodzi. Ndipo ichi ndi chinthu chimene ine ndikufuna kuti ndichifikitse kwa inu, mwaona, kuti ife sitiri kwenikweni ogawanika. Ife ndife miyala yomwe yadulidwa mu mawonekedwe osiyana, yonse kwa ulemerero wa Mulungu.

13 Tsopano, ziripo zochuluka kwambiri mu tsiku lomwe tiri kukhalamo, zokhudzana ndi "mphatso." Anthu ochuluka kwambiri amawaweruza anthu ndi mphatso zomwe iwo ali nazo. Chabwino, ine ndikukhulupirira kuti zinthu izi ndi mphatso. Ine ndikukhulupirira kuti zomwe ife timaziwona zikuchitika ndi mphatso, ndipo izo ndi mphatso zopatsidwa ndi Mulungu. Koma, ife, ngati ife sitizigwiritsa izo mwa njira yoyenera yomwe Mulungu analinga kuti izo zizigwiritsidwira, ndiye ife tikhoza kuchita zopweteketsa kwambiri ndi mphatso kuposa momwe ife tikanakhoza ngati ife tikanati tisakhale nazo mphatso. Usiku wina ine ndinapanga neno paguwa, kunena izi, kuti ine kulibwino ndiziwona chikondi chapaabale chiripo pakati pa mpingo, ngati ife tikanati tisakhale ndi kuchitika kumodzi kwa machiritso kapena china chirichonse. Mwaona, ife tiyenera kumadziwa kuti zinthu izi nzanji.

14 Tsopano, ngati munthu abwera ndipo iye ali nayo mphatso yaikulu, ziribe kanthu ngati iye ali wa chipembedzo chathu kapena chipembedzo china, musati mumuweruze iye ndi chipembedzo chomwe iye akuchokerako, momwe iye akuvalira, koma chimene inu mukufuna kuti muwone ndi chimene iye akuyesera kuti achite nayo mphatso imeneyo. Cholinga chomwe iye ali nacho. Ngati iye akuyesera kuti atenge kukopa kwake ndi kudzimangira yekha dzina lalikulu kuchokera pa iyo, ine ndingakhale nako kuuzindikira mzimu mokwanira kudziwa kuti icho ndi cholakwika. Ziribe kanthu momwe iye aliri mphunzitsi wamkulu, momwe iye aliri wamphamvu, momwe iye aliri waluntha, kapena momwe mphatso yake imagwirira ntchito, ngati iye sali kuyesera kukwaniritsa chinachake kwa phindu la Thupi la Khristu, kuzindikira kwako komwe kwauzimu kungakuuze iwe kuti uko nkulakwitsa. Ziribe kanthu ndi zolondola bwanji, zangwiro bwanji, momwe izo ziriri, ndi zolakwika ngati iyo silikugwiritsidwira kwa Thupi la Yesu Khristu.

15 Kuti ukwaniritse chinachake, mwina iye ali ndi mphatso yaikulu yomwe iye angakhoze kuwakokera nayo anthu palimodzi ndi luntha lalikulu kapena mphamvu yauzimu, yomwe iye angakhoze kuwakokera anthu palimodzi, ndipo mwina iye akuyesera kuti atenge mphatso imeneyo ndi

kudzipangitsa yekha kutchuka chotero kuti iye akhale nalo dzina lalikulu, chotero kuti abale ena aziyang'ana pa iye ngati munthu wina wamkulu. Ndiye uko nkulakwitsa. Mwinamwake iye akuyesera ku—kuti amangirize chinthu chinachake pano chimene iye akufuna wina aliyense achoke pa chithunzi ndi kudzilola iye ndi gulu lake akhale chithunzi. Uko nkulakwitsabe, mwaona.

16 Koma ngati iye ali nayo mphatso ya Mulungu ndipo iye akuyesera kulimangiriza Thupi la Khristu, ndiye ine sindikusamala kuti iye ndi wa kuti. Inu simukumuzindikira munthuyo, inu mukuuzindikira mzimu, moyo umene uli mwa munthuyo. Ndipo ndicho chimene Mulungu anatiuza ife kuti tizichita. Palibe nthawi imodzi yomwe ife tinatumidwa kuti tizikalizindikira—gulu la munthu. Koma ife tinakakamizidwa ndi kulamuliridwa ndi Mulungu kuti tiziuzindikira mzimu uli mwa munthu, chimene iye akuyesera kuti achichite, chimene mzimu mu moyo wake ukuyesera kumutsogolerako iye. Ndiyeno ngati ife tingakhoze kupeza kuti iye akuyesera kuwatsogolera anthu (osati kuti awaphwasule iwo, koma kuti awabweretse iwo palimodzi) ndi kuwubweretsa Mpingo wa Mulungu wamoyo, osati onse ku chipembedzo chimodzi, koma ku kumvetsa, chiyanjano, umodzi wa mzimu. Ndiye ngati iye ali mvula yanyundo kapena mvula yamasika, kapena chirichonse chomwe icho chiri, mzimu wake ndi cholinga chake ziri zolondola. Ndipo mzimu umene uli mwa iye, ziribe kanthu kuti iye ndi wa gulu lanji, Mzimu umene uli mwa iye ukuyesera kuwalozera anthu ku Gologota, kuchoka kwa iyemwini kapena kuchoka kwa china chirichonse, koma chopindula chake chokha chomwe iye ali nacho ndicho kuwalozera iwo ku Gologota. Iye samasamala kaya iye akudziwidwa kapena ayi. Iye samasamala kaya ngakhale gulu lake lomwe. . . zomwe ziri zabwino, mwaona, ndi zabwino, ngati iye ali wa Chimethodisti, kapena wa Chipresbateria, kapena Roma Katolika, kapena chirichonse chimene iye akufuna kuti akhale mwa chipembedzo.

17 Koma kodi iye akuyesera kuchita chiani, mwa cholinga cha mtima wake chimene iye akuyesera kuti achipeze? Ndiye inu mukhoza kuwona chimene chiri mu moyo wa munthu, kaya zolinga zake ziri za chake—chipembedzo chake, kaya ndi za iyemwini, kaya ndi za zinthu zachidziko, kaya ndi za maina aakulu, kuti aziti, "Ine ndinaneneratu izo, zinabwera nkudzachitika ndendende." Tsopano, inu mukuona ndiko kulakwitsa apo pomwe, pa kuyamba nazo. Koma ngati iye akuyesera kuti agwiritse ntchito chimene Mulungu anamupatsa iye, monga mphunzitsi, monga mneneri, monga mpenyi. . .

18 Mneneri wa Chipangano Chatsopano ndi mlaliki. Ife tonse tikudziwa izo. Mtumiki aliyense basi yemwe ali mlaliki ndi mneneri, mneneri wa Chipangano Chatsopano, ngati iye akulosera, akulalikira, osati kuti aziyesera kudzimangiriza

iyemwini kuti apange dzina lalikulu, kapena kuti amangirize bungwe lake. Chimene, iye ayenera kuti akhale mu bungwe. Ine ndiri pano wopanda limodzi, komabe pomalalikira inu muyenera kukhala muli. Ndiko kulondola. Munthu aliyense ayenera kukhala nawo mpingo wa kwawo. Inu muyenera kukhala ndi malo, osati kumangoyandama kuchokera ku msanamira kupita ku mtengo, koma muzikhala ndi kwinakwake kumene inu mumapita ku mpingo ndipo inu mumautcha iwo mpingo wanu, kwinakwake kumene inu mumalipira chakhumi chanu, ndi kwina kumene inu mumathandizira Cholingacho. Mutenge kusankha kwanu, komano musati muzimuchotsa mchiyanjano munthu winayo chifukwa iye sali mu gulu lanu. Mwaona? Kuuzindikira mzimu wake ndi kuona ngati iye ali nacho cholinga chomwecho mu mtima, ndiye inu muli nacho chiyanjano wina ndi mzake. Inu mukugwirira ntchito kwa Cholinga chimodzi chachikulu. Ndicho cholinga cha Khristu. Ine ndikuganiza kuti izo ndi zoona mwamtheradi.

19 Tsopano, ngati ife titi tizindikire zolinga ndi zokhumba za aneneri Achipangano Chakale, amuna awo anali ndi cholinga chimodzi, ndipo icho chinali Yesu Khristu. Iwo anali ndi chinthu chimodzi chomwe nkhani yonse ya Chipangano Chakale inamangidwa mozungulirapo, Mesiya wakudza. Iwo—iwo sankapita kunja ndi kukachita zinthu basi pofuna ndalama kapena pofuna kutchuka. Iwo anali ndi chinthu chimodzi, iwo anali odzozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, ndipo iwo ananeneratu za Mesiya wakudza. Ndipo amuna awo anali odzozedwa kwambiri ndi Mzimu mpaka nthawizina iwo ankachita monga Mzimu umene unali mkati mwa iwo, iwo ankayankhula mooneka za ngati iwoeni. Taonani momwe Mzimu wa Mulungu unkawapangitsira amuna amenewo kuchita.

20 Ife titenge, mwa chitsanzo, Mose, mneneri wamkulu, momwe kuti munthu ameneyo analibe zolinga zodzikonda nkomwe. Iye akanakhoza kudzakhala mfumu ya Igupto. Iye akanakhoza kudzakhala ndi dziko pansi pa mapazi ake. Koma chifukwa chakuti iye anali mneneri mu mtima, iye anakana kuti azitchedwa mwana wa mwana wamkazi wa Farao, kusankha maka kuti avutike chisautso ndi mayesero a Khristu, kuwerengera chuma cha Kumwamba ngati chuma chachikulu kuposa icho cha Igupto. Iye anakana ndipo anadzikaniza yekha kutchuka kwa mdziko, kupezabwino ndi—zinthu zomwe moyo umapereka. Iye ayenera kuti ankayang'ana kupyola izo. Mukuona, iye—iye akanakhoza kudzakhala zimenezo.

21 Mungomutenga mtumiki lero, ngati iye ali nao ubatizo wa Mzimu Woyera, ndipo iye akudziwa kuti ngati iye azilalikira Mawu awo, izo zidulira kutchuka kwake pansi; izo zimuika iye mu mpingo waung'ono kwambiri kwinakwake, kapena mwina kunja pa msewu. Koma iye amadziwa kuti chinachake mu mtima mwake chikuyaka. Iye amakuwona Kudza kwa Ambuye.

Iye sasamala kuti kaya iye ali ndi mpingo waukulu kapena mpingo waung'ono. Iye samasamala kaya iye ali ndi chakudya cha lero kapena alibe chakudya ayi. Iye samasamala kaya iye ali ndi zovala zabwino kapena iye alibe zovala zabwino. Iye amangokhala wosamalitsa za chinthu chimodzi, ndipo ndicho Moyo womwe mkati mwa iye ukulirira uko. Iye akuyesera kuti apindulire chinachake kwa ulemerero wa Mulungu, ndipo munthu uyo, pakuchita chotero, amachita Moyo womwe wa Mzimu umene uli mwa iye. Kodi inu mukunditsatira ine? Iye amachita za iwo.

22 Tayang'anani pa Mose pamene iye anafika pa nthawi yomwe iye anawonetsera, moyo wake wonse unali Mzimu wa Khristu, pakuti Khristu anali mwa iye. Khristu anali mwa Mose, mwa muyezo. Tsopano, ngati ife titazindikira, iye anabadwa mu nthawi ya chizunzo. Ana anaphedwa poyesera kuti amupeze iye, ndendende basi monga iwo anachitira ndi Yesu. Ndipo ife tikupeza kuti pamene iye anafika pa malo akuti ana a Israeli sanamvere mwanjira yoteroyo mpaka Mulungu anali wokwiya nawo, ndipo Iye anati kwa Mose, "Pita pambali ndipo ine ndiwononga gulu lonse la iwo, ndipo ine nditenga a iwe ndi kuwutsapo m'badwo wina."

23 Mose anadziponyera yekha mu njira ya chiweruzo cha Mulungu, ndipo anati, "Munditenge ine Inu musanati muwatenge iwo." Mwa kuyankhula kwina, "Inu musanati muwatenge iwo Inu muyenera mudutse pamwamba pa ine."

24 Ndizo ndendende zomwe Yesu Khristu anachita. Pamene Mulungu akanasesa pa nkhope yonse ya dziko lapansi ochimwa awa, inu ndi ine, koma Khristu anadziponyera Yekha mu njira. Mulungu sakanakhoza kuchita izo, Iye sakanakhoza kubwera pa Mwana Wake yemwe.

25 Ndipo pamene Mulungu anawuona Mzimu umenewo mwa Mose, utapachikika mu chiweruzo monga mtanda apo, "Inu simungakhoze kubwera kwa iwo, Inu muyenera kuti munditenge ine poyamba," mukuwuona Mzimu wa Mulungu mwa Mose? Pamene iye akanakhoza kukhala mfumu ya Igupto, pamene iye akanakhala nazo zawofuwofu zonse za mdziko, kuti akhale wotchuka, pamene iye akanakhoza kukhala mfumu yaikulu ya mdziko pa nthawi imeneyo. Koma iye anasankha kuti avutike mazunzo ndi zowawa, pakuti iye anachiwerengera chitonzo cha Khristu ngati chuma chachikulu kuposa icho cha Igupto. Inu mukuona, iye anadziponyera yekha mu njira. Chifukwa? Uja anali Mulungu mwa Mose anachita izo. Kuganiza kwabwino, munthu waluntha sakanachita konse izo, iye akanadzatenga njira yophweka. Chotero ziribe kanthu momwe Mose ankawoneka wotentheka mochuluka, iye anali kuyesera . . . Inu mukuona, iye anali mneneri woona wa Mulungu, chifukwa iye anali kuyesera kuti apindulire chinachake kwa Ufumu wa Mulungu.

26 Tsopano, ndi mphatso yake yaikulu ya ulosi iye mwina akanakhala munthu wanzeru, akanakhoza kumaima mu Igupto ndi kuti, "Tsopano dikira, ine ndilosera zakuti-n-zakuti. Ine ndinena zakuti-n-zakuti," ndipo monga ndi ulosi wake. Koma ziri . . . ndi, o, iye akanakhala ali wotchuka-padziko. Koma izo sizinali mu mtima wake. Izo sizikanakhoza kukhala ziri mu mtima wake.

27 Chotero ngati inu mumuwona munthu ali ndi mphatso yaikulu, akuyesera kuti achite chinachake kuti adzipatse yekha ulemerero, kuuzindikira kwanu komwe kwa mzimu kumakuuzani inu kuti izo ndi kulakwitsa. Koma Mose anali kuyesera kuti akwaniritse chinachake kwa ulemerero wa Mulungu. Ziribe kanthu kaya izo zinali moipa bwanji; kaya momwe izo zinkawoneka zaudierekezi, kaya momwe izo zinkakambidwa mochuluka, Mzimu mwa Mose unamulondolera iye molunjika ku mzere wa ntchito. Mzimu mwa iye!

28 Tayang'anani pa Yosefe, Yosefe anali . . . pamene iye anabadwa, iye ankakondedwa ndi atate ake ndi kumadedwa ndi abale ake, choimira changwiro cha Khristu. Ndi chokha . . . iye anali m'bale wamagazi kwa iwo, bambo yemweyo. Koma chifukwa chimene abale ake ankamuda iye, mopanda chifukwa, nchifukwa Mulungu anali atamupanga iye mneneri, wauzimu, mpenyi. Ndipo iwo ankamuda iye chifukwa cha cholinga icho chomwe. Koma Yosefe sakanakhoza kuzithandizira izo, chifukwa, Mulungu anali atamupanga iye mwanjira imeneyo.

29 Ndipo upenyeni Mzimu wa Mulungu mwa Yosefe. Penyani zomwe iye anachita. Iye anachita ngakhale gawo la Khristu. Iye anadedwa ndi abale ake, ankakondedwa ndi abambo ake, chifukwa Mzimu unkapangitsa kusiyanako. Iye anali munthu wauzimu. Iye ankawona masomphenya, iye ankatanthauzira maloto. Iye sankachita izo kwa ulemerero wake wake. Iye ankachita izo chifukwa panali chinachake mwa iye, Mzimu wa Mulungu. Iye sakanapita kumeneko mwa iye yekha, ndi kukaponyedwa mu dzenje, ndi kuwapangitsa bambo ake okalamba kumadandaula zaka zonse izo, kugulitsidwa kwa pafupi zidutswa sate za siliva; kuchotsedwamo mu dzenje, ndipo anadzakhala munthu wakudzanja lamanja la Farao, mfumu ya dziko lapansi pa nthawi imeneyo. Ndipo mu nyumba yake ya ndende uko kunali woperekera chikho ndi wophika mkate, ndipo mmodzi anataika ndipo winayo anapulumutsidwa, mwa kuneneratu kwake, mu nyumba ya ndende.

30 Ndipo kodi inu munazindikira Yesu pamene Iye anabwera, Iye ankakondedwa ndi Atate. Ndipo atate anamupatsa Yosefe chikhoto cha mitundu yambiri (utawaleza, pangano). Ndipo Atate, Mulungu, anapereka Mwana wake, Yesu, pangano, ndiyeno m'bale Wachiyuda ankamuda Iye popanda chifukwa. Iye analibe chifukwa chomudera Iye, Iye anali wauzimu, ndipo Iye anali Mawu a Mulungu atawonetseredwa. Iye

anabwera kudzachita chifuniro cha Atate, Iye anabwera kuti adzakwaniritse Malemba. Iye anabwera kuti adzawabweretsere iwo mtendere, koma iwo sanamumvetse Iye, ndipo ankamuda Iye popanda chifukwa. Iwo sanati aime kuti ayese kuona zomwe Iye anali kuyesera kuti apindule. Iwo ankangomuweruza iye chifukwa chakuti iye sankagwirizana nawo iwo. Iwo anapanga . . . "Iye akudzipanga Yekha chakuti-n-chakuti. Iye akudzipanga Yekha Mulungu." Iye anali Mulungu! Mulungu anali mwa Iye. Baibulo linati Mulungu anali mwa Khristu, akudziwonetsera Yekha kwa dziko. Iye anali Mulungu wa Ulemerero akuwonetsera ulemerero wa Mulungu.

31 Tayang'anani pa Mose, iye sakanachitira mwina kudziponyera yekha apo. Iye sanachite izo mwachinyengo. Iye anachita izo chifukwa Mulungu anali mwa iye. Ngakhalenso Yosefe sakanachitira mwina chomwe iye anali, chifukwa uyo anali Mulungu mwa iye akugwira ntchito kapena akudziwonetsera yekha kupyolera mwa munthu. Sikuti iye ankachita izo kwa ulemerero-wayekha.

32 Munthu aliyense yemwe . . . Ngati ansembe aja akanakhala nako kokha kuuzindikira mzimu, monga ine ndinali kuyankhula kwa inu mmawa uno. Mosasamala za momwe dziko linkayankhulira za Iye, iwo apobe akanadziwa ngati iwo akanati ayang'ane ku Mawu, ngati iwo akanati awone cholinga Chake. Iye anali nthawizonse akuchita izo kuti apereke ulemerero kwa Atate. Iye anati . . . Iwo anati, "O, munthu uyu ndi mchiritsi wamkulu, Iye amachita zinthu izi monga choncho."

33 Iye anati, "Ine sindimakhoza kuchita kanthu mpaka Atate atandiwonetsera Ine. Si Ine amene ndikuchita ntchitozo. Ndi Atate amene akukhala mwa Ine, Iye akuzichita ntchitozo." Iye sanadzitengere konse ulemerero.

34 Sakanatinso wantchito aliyense wa Mulungu atenge ulemerero. Sakanatinso wantchito aliyense wa Mulungu atenge mphatso ya Mulungu ndi kuyesera kuti adzipatse ulemerero yekha, kapena china chirichonse, koma chopindula chake cholondola chiri kuti achite chinachake kwa ulemerero wa Mulungu. Ndicho chifukwa inu mukuona chinthu chomwecho lero. Ife tiyenera kumakhala nako kuuzindikira mzimu, kuti timuwone munthu chimene iwo akuyesera kuti achite. Kodi iwo akuyesera kumupatsa ulemerero Mulungu? Kodi iwo akuyesera kudzipatsa ulemerero okha?

35 Tsopano Mzimu wa Mulungu ukamagwira ntchito mwa munthu umampangitsa munthu kumachita monga Mulungu. Nzosadabwitsa Yesu anati, "Kodi izo sizinalembedwe, 'Inu ndinu amulungu'? Ndipo ngati iwo ankawatcha iwo 'amulungu,' kwa omwe Mzimu wa Mulungu unkabwerako, inu mungandinyoze bwanji Ine, ndiye, pamene ine ndiri Mwana wa Mulungu?" Ngati inu mungakhoze kuwuona Mzimu wa Mulungu

mwa Mose, chimene, iye anali mulungu. Mose anali mulungu. Yosefe anali mulungu. Aneneri anali amulungu. Baibulo linati iwo anali. Iwo anali amulungu chifukwa iwo . . . iwo anali atadzipereka okha kwathunthu kwa Mzimu wa Mulungu, kuti iwo anali akugwira ntchito mwa ulemerero wa Mulungu.

36 Ndipo pamene munthu ali wodzozedwa kwambiri ndi Mzimu . . . Tsopano mulole izi zipite mwakuya kwenikweni pansi pa nthiti yachisanu ku mbali ya kumanzere. Pamene munthu ali wodzozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, zizolowezi zake, zochita zake, ndi chirichonse, ndi Mulungu akuchita mwa iye. Nthawizina iye amaweruzidwa molakwika.

37 Tayang'anani pa Davide, mu Salmo ya 23, iye analira, "Mulungu wanga, Mulungu wanga, nchifukwa chiani inu mwandisiya ine?" ngati kuti iye anali, ngati Davide anali munthuyo. "Onse omwe akundidutsa ine, akupotoza milomo kwa ine."

38 Iye anali atadzozedwa kwambiri ndi Mulungu, iye anali atadzipereka mwangwiro kwambiri kwa Mulungu, ndipo kudzozako kunali pa iye mwanjira yotero ndipo pamene iye ankalira ndi Mzimu wa Mulungu, ngati wina akanakhala ataima pamenepo, akanati, "Bwanji, taonani, iye akuganiza kuti winawake anapotozera milomo kwa iye. Nchifukwa chiani Mulungu wamusiya iye?"

39 Uyo sanali Davide, uwo unali Mzimu ukulira mofuula kupyolera mwa Davide. "Mulungu wanga, Mulungu wanga, nchifukwa chiani inu mwandisiya ine? Mafupa anga onse akuwonekera pa ine. Iwo alasa manja anga ndi mapazi anga."

40 Chabwino, wina anati, "Mvetserani kwa wachinyengo uyo kumtunda uko. Manja andani omwe alasidwa? Mapazi andani alasidwa?" Ndiwo aluntha.

41 Koma yemwe anali atauzindikira mzimu anadziwa kuti uwo unali Mzimu wa Mulungu mwa iye ukulira mokweza. Pamene munthu ali wodzozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, iye amachita ndi machitidwe a Mulungu, ndipo machitidwe a Mulungu si oti azitiswa ife pano. Kuchita kwa Mulungu ndi koti kutikokere ife palimodzi pakuti ife ndife amodzi mwa Khristu Yesu, ndipo cholinga cha Mulungu nchoti atibweretse ife palimodzi. "Kukondana wina ndi mzake."

42 Tsopano, aneneri aakulu awo, ife tikuwona Mzimu ukusuntha mwa iwo, Yesu anawatcha iwo "amulungu." Iye anati iwo anali amulungu. Tsopano pamene Mzimu umadza kwa iwo mwa muyezo, koma pamene iwo unadza pa Mmodzi, Yesu, yemwe anali Mwana wa Mulungu, iwo unadza kwa iye mopanda muyezo, chidzalo cha Umulungu mwathupi chinali mwa Iye, pakuti Iye anali chitsanzo changwiro. Iye anali Mulungu wa Ulemerero akuwonetsera ulemerero wa Mulungu kwa anthu, Mulungu mwa Iye akupita uku ndi uko. Penyani moyo Wake,

Chipangano Chakale chonse, Iye anali nkhani ya Chipangano Chakale. Aneneri onse akale mmbuyo mu Chipangano Chakale ankafuulira apo, osati kwa iwoeni, iwo ankafuula pansi pa Mzimu wa Mulungu, ukuwapanga iwo kumachita monga Mulungu mochuluka kuti iwo ankatchedwa amulungu, ndiyeno chidzalo cha Mzimu umenewo chinawonetseredwa mwa Yesu Khristu.

43 Tayang'anani pa Davide pamene iye anachotsedwa pa mpandowachifumu monga mfumu ya Israeli, atakanidwa ndi anthu ake omwe, akupita chokwera Phiri la Azitona, kumpoto kwa Yerusalemu, ndipo iye anayang'ana mmbuyo pa mzinda ndipo analira chifukwa iye anali atakanidwa. Chinali chiani icho? Uwo unali Mzimu wa Khristu.

44 Zaka mazana asanu mtsogolo, Mwana wa Davide, Yesu, anakhala pa phiri lomwelo, akuyang'ana pa mzinda, ngati mfumu yokanidwa, ndipo analira, "Yerusalemu, Yerusalemu, ndi kangati ine ndakusonkhanitsa iwe (zipembedzo zanu zosiyana ndi chirichonse) monga nkhuku ichitira pa anapiye ake, koma iwe sukufuna ayi. Ndi kangati ine ndazichita izo!"

45 Tsopano Mzimu womwewo umene unali mwa Davide, umene unawonetseredwa mwa chidzalo mwa Khristu, uli mu Mpingo lero ukulirira kwa anthu. "Ndi kangati ine ndingakusonkhanitseni inu!" Ndipo pamene inu mukuwona kupatukana ndi—ndi zosiyana ndi—ndi ubale ukusweka, ndi moyo wa Chikhristu, wina kutsutsa mzake, ndiye izo zimapangitsa Mzimu wa Mulungu mu mtima mwanu kulira mofuula. Inu mukuyesera kukwaniritsa chinachake, mneneri woona wa Mulungu, mphunzitsi woona akuyesera kuti awubweretse Mpingo ku chiyanjano cha mzimu, chiyanjano cha mzimu, kuti iwo akhoze kumuzindikira Mulungu; kuyesera kuti akwaniritse izo ziribe kanthu achipembedzo chomwe ali a icho kapena chiani chokhudza izo. Ife tiri nako kuzindikira kwa mzimu kuti tiuzindikire mzimu umene uli mwa munthuyo, kuti tiwone ngati iwo uli Mzimu wa Mulungu kapena ayi.

46 Tsopano, ife tikuzindikira pamene Iye anali pano pa dziko lapansi, momwe Iye ankapitira uku ndi uko akuchita zabwino. Ine ndinazindikira chinthu china chimene chikudza ku malingaliro anga. Kodi inu munazindikira pamene Davide anakanidwa ngati mfumu? Iye anapita kunja kwa mzinda, ndipo wachi Benjamini wamng'ono, wachi Benjamini, yemwe ankayenera kuti akhale ali m'bale kwa iye, akanayenera kuti akhale wachisoni chifukwa iye anali atakanidwa, koma chiani...Iye anali munthu wolumala. Ndipo iye anazikhwakhwaza cha kumeneko ndi chikhalidwe chake cholumala, akuponyera dothi pa Davide, ndi kumamutcha iye mitundu yonse ya maina oipa, ndi kumamutukwana iye mu Dzina la Ambuye, kumamutukwana Mfumu Davide mu

Dzina la Ambuye, wachikulire wachi Benjamini wamng'ono wolumala uyu.

47 Penyani Mzimu wa Mulungu ndi mzimu wa Mdierekezi ukugwira ntchito. Tsopano, ngati inu mutazindikira, iye anali wopuwala. Izo zikuimira kulumala kwauzimu kwa anthu lero omwe angati aselewule kwa Mzimu woona wa Mulungu mwa Khristu ukudziwonetsera Wokha. Uwo unali Mzimu wa Khristu mwa Davide ukukanidwa ngati mfumu. Ndipo, lero, pamene anthu akuwaseka anthu omwe alandira Mzimu Woyera ndi kumayesera kuti apindule chinachake, kuti awakokere Achimethodisti ndi Apentekoste, ndi Abaptisti ndi Apentekoste, Achipresbateria ndi onse, limodzi ngati chiyanjano, monga Thupi la Khristu, ndipo iwo amauwona Mzimu ukugwira ntchito, amati, "Chabwino, taonani, ndi wa Chipentekoste. Kutali ndi iye! Ine ndikudziwa wina anathawa ndi mkazi wa mwamuna wina. Ine ndikumudziwa uyu analedzera. Ine ndikumudziwa uyu anachita *ichi*. Ine ndikumudziwa uyu anachita *icho*." Zonse izo, koma iwo ndi aakulu mokwanira kuti azibisa zinthu zawo zomwe, iwo akhoza kuzibisa izo. Koma Davide anayalutsidwa. Chifukwa chiani? Iye anali ndi Mzimu wa Khristu mwa iye.

48 Mlonda uja anati, "Kodi ine ndiutenge mutu wa garu uyo yemwe akutukwana mfumu yanga?"

49 Penyani Mzimu wa Khristu mwa Davide, "Msiyeni iye yekha, pakuti Ambuye amuuza iye kuti anditukwane ine." Kodi inu mukumvetsa izo? "Msiyeni iye yekha, Ambuye amuuza iye kuti anditukwane ine."

50 Mmalomwake, lero, ife timafuna tiimike zibakera zathu ndi kumenyana naye, mwaona, kuudula mutu wake, "Eya, mchotseni iye, iye sali wa ife."

51 "Msiyeni iye yekha, Ambuye amuuza iye kuti anditukwane ine." Wolumala wamng'ono uyo akuthamanga motsatira apo, akuponyera dothi pa Davide.

52 Ndizo zomwe iwo akuchita lero pa Mzimu wa Khristu. "Iwo ndi gulu la oyera odzigudubuza. Iwo ali—iwo ndi gulu la *izi*. Palibe kanthu kwa iwo. Palibe kanthu kwa machiritso Auzimu. Kulibe chinthu chotero chonga Angelo. Kulibe chinthu chotero chonga aneneri." Zinthu zonse izo, "Masiku a zozizwitsa anatha," kumaponyera dothi. Koma asiyeni iwo okha! Koma pamene Davide anabwerera mu mphamvu, aleluya, pamene iye anabwerera ngati mfumu yathunthu ya Israeli . . . Musati mudandaule, Yesu uyu, Mzimu Wake womwe ife tiri nawo lero, anachita gawo Lake natsiriza, adzabwerera kachiwiri mu thupi logwirika, nthawi yachiwiri, mu ulemerero, mu mphamvu ndi mu ufumu.

53 Woponya zibuluma wamng'ono uja anagwa pa nkhope yake ndipo anapempha chifundo. "Msiyeni iye yekha," Mzimu wa

Khristu mwa ife. Musati mumuchotse iye. Tiyeni tikumbukire kuti zinthu zonse izi ziyenera kufika pochitika. Ife tiri nacho chinthu chimodzi choti tichite, kusunthira chitsogolo. Mulungu analonjeza kuti Iye akanadzapangitsa chirichonse kugwira ntchito limodzi kwaubwino wa iwo amene amamukonda Iye. Tiyeni tisunge kuzindikira kwa mzimu, tisunge cholinga molondola. Ife tiri kuno kuti tizimutumikira Mulungu, aliyense kumayanjana, kumapitirira ndi kumamutumikira Mulungu. Ngati munthu ali ndi cholinga cha mtundu wolakwika, ndiye nchiani chiti chichitike? Mwaona?

54 Tsopano, ife tikupeza kuti Mzimu wa Mulungu unali mwa Iye. Aneneri onse akale ankayankhula za Iye. Mizimu yonse, mwa kagawo, kagawo kakang'ono kalikonse, sanali kudzipatsa mwiniwake ulemerero (aneneri owona), aneneri onse owona anali ananena Iye, ankayankhula za Iye. Ndipo zirizonse zomwe iwo anayankhula zinakwaniritsidwa mwa Iye. Zinasonyeza kuti unali Mzimu wa Mulungu mwa iwo, izo zinakwaniritsidwa. Chinali chiani icho? Mulungu akuyankhula za Iyemwini. Mwaona? Mulungu akudziwonetsera Yekha kupyolera mwa aneneri awa.

55 Osati kutenga ulemerero, "Ndani ati akhale Purezidenti wotsatira? Ndi ndani ati adzakhale ichi?" Ndi kukumenya iwe pa mutu, "Tiuze ife ndani wakumenya iwe ndipo ife tikukhulupirira iwe." Izo si ndizo. Ndi chinachake kuti tiwonetsere Mulungu. Izo sichinachake choti chimupange M'bale Weathers pano, kapena M'bale Shores, kapena M'bale Wakuti-n-wakuti kunja uko, munthu wamkulu, ndi kumupanga iye wamkulu kuposa munthu aliyense wa gulu lino, kumupanga iye munthu wamkulu kwambiri mu Phoenix. Izo si kumupanga William Branham chinachake chachikulu. Koma nchiani choti tichite? Icho si kumupanga Oral Roberts chinachake chachikulu, Billy Graham chinachake chachikulu. Koma ndi mitima, ife tikuyesera kuti tipindulire chinachake kwa Ufumu wa Mulungu. Ndi kuwonetsera Mulungu. Mphatso zonse ndi zinthu sizimamupanga wina kukula kuposa mzake, izo zimangotipanga ife tonse kugwirira ntchito limodzi popangitsa ungwiro wa thupi, kuti atibweretse ife tonse palimodzi ngati anthu amodzi, ngati anthu a Mulungu. Koma pamene inu muwawona iwo akupita mosiyana, musati muziwatemberera iwo; muzingowasiya iwo okha, winawake ayenera kuchita izo. Koma dikirani mpaka Yesu abwere mu mphamvu.

56 Tsopano ife tikuwawona aneneri onse awo akuyankhula. Wina aliyense wa iwo anali kumupatsa ulemerero Mulungu ndi Mesiya wokudza. Ndipo pamene iwo analowa mu Mzimu, iwo ankachita ndipo ankayankhula ndi kumakhala moyo basi monga Mesiya ankachitira. Ngati izo zinachitika mbali iyo ya mtanda, kukamba za kudza Kwake, ndi mochuluka bwanji izo ziti zidzakhale ziri kutachitika kudza Kwake, zidzauika Mzimu

wa Mesiya mu Mpingo kuti uzichita, kupanga, kugwira ntchito, ndi kukhala moyo monga Mesiya? Ndi Mzimu wa Mulungu.

57 Muuzindikire mzimu umenewo, muwone ngati iwo uli wa Mulungu kapena ayi. Muwone ngati iwo ukuchita monga Iye. Muwone ngati zotengeka zanu. . . Ngati wina akankha chinachake motsutsa inu ndi kuponyera dothi pa moyo wako, ndipo iwe ukudziwa kuti ndiwe wosalakwa monga iwe ungakhoze kukhalira, ndipo iwe ukudziwa kuti iwe uli nawo Mzimu wa Mulungu, usati uyesere kudzipatula wekha. Usati uyesere kuchita moyipidwa kwa iwo. Usati uwatemberere iwo. Ingomayenda, kumadziwa kuti Mulungu anachita izo kuti akupatse iwe chiyeso kuti awone momwe iwe ukadatengera izo. Iye adzayenera kuti abwere kwa icho mulimonse.

58 Monga ine ndinanena tsiku lina, ine ndikukhulupirira mu mpingo wa M'bale Fuller, za wokwera njinga mu Canada. Chabwino, onse a iwo ankaganiza kuti iwo angakwere momuposa mnyamata uyu, basi wachikazi wachikulire wamng'ono. Ndipo iye anali mmodzi yekha yemwe sakanakhoza kukwera mopanda kugwirira zigwiriro.

59 Ndine wokondwa ine ndimakonda kuti ndikhale mmodzi wa okwera akale azigwiriro, kugwira mbali zonse za Mtanda ndi kuti, "Palibe kanthu mmikono mwanga ine ndikukabweretsa. Ndiroleni ine ndigwirizire ku Mtanda, Ambuye, ine ndiribe luntha ayi. Ine ndiribe kanthu. Ndiroleni ine ndingogwira apa, ndiyang'ane kunja kutali uko."

60 Ndipo iwo anali ndi thabwa la mainchi thwelofu kuti azikwerapo mtunda wa mdadada wa mu mzinda, kuti akatenge njinga ya Schwinn ya handiredi dolla. Anyamata onse awo amene amakhoza kukwera popanda kugwirira, amapita kumusi ndi kukatenga za mgolosare za amayi awo ndi kumabwerera popanda ngakhale kugwira chiongolero, iwo aliyense anayamba kuyang'ana. Iwo sanali ozolowera kugwirira ziongolero, ndipo iwo anagwapo. Koma mnyamata wachikulire pang'ono uyu anakwera apo ndipo anagwirira ziongolero ndi kuyikwera iyo mpaka ku mapeto. Iwo anamufunsa iye, anati, "Iwe wachita motani izo?"

61 Iye anati, "Apa ndi pamene inu munapanga kulakwitsa kwanu, anyamata. Ndinu nonse okwera bwino kuposa momwe ndiriri, koma inu mumayang'ana apa," ndipo anati, "zinakupangani inu manjenje poona zomwe. . . Inu mumayesera kudzibalanitsa nokha, ndipo inu munagwapo." Anati, "Ine sindimayang'ana nkomwe *apo* monse, ine ndimayang'ana mapeto ndipo ndimapita modekha."

62 Ndicho chimene ife tikuyenera kuti tizichita. Musati muziyang'ana kwa zinthu zazing'ono izi tsopano, "Kodi mmodzi uyu anachita *izi* kapena mmodzi uyo anachita *izo*?" Muziyang'ana mapeto ndipo muzingokhalabe odekha. Khristu

akubwera. Muziyang'ana mapeto, muzingokhalabe odekha. Musati muzizindikira zomwe zikuchitika tsopano. Muzipenya zomwe ziti zikachitike ku nthawi yotsiriza, pamene ife titi tidzaime ndi—ndi kulongosola nkhani ya miyoyo yathu.

63 Davide sanali kuyang'ana wachi Benjamini wachikulire pang'ono akuponyera dothi pa iye, iye anali wolumala mulimonse. Iye sankasamala konse za iye. Iye sakanamulola ngakhale mlonda kuti adulepo mutu wake, anati, "Msiyeni iye yekha, Mulungu wamuuza iye kuti achite izo. Mulungu wamuuza iye kuti anditukwane ine, msiyeni iye yekha." Pakuti Davide ankadziwa kuti tsiku lina iye anali kubwerera mu mphamvu. Wachi Benjamini uja akanadzakhala ndi nthawi yake.

64 Inde, ndi zimenezo. Mpingo udzauka mwa chigonjetso. Ine ndinatumizidwa kokha kuti ndizidzapempherera ana Ake odwala, basi. Ndi zonse zomwe ine ndingakhoze kuzichita. Konse komwe iwo ali ndi mpingo womwe iwo alimo, izo sizimandipanga ine kukhala wosiyana. Ine ndikuyesera kuti ndiziwapempherera ana Ake odwala, kuyesera kuwonetsera mphatso kwa ulemerero Wake. Ndicho chifukwa ine sindinakhale konse wa ku chirichonse.

65 Tsopano, kumbukirani, izo zonse nzabwino. Mwaona, ine sindiri—ine sindikunena izo tsopano. Ine ndikufuna inu mundimvetse ine momveka kuti ine ndimakhulupirira kuti Mulungu ali nawo Akhristu mu mpingo uliwonse, ana Ake. Iye sanandifunsepo ine pa izo. Ine ndinangotumizidwa kuti ndizikawapempherera ana, ndi kumachita zinthu izi, ndi kumamuwonetsera Iye.

66 Tsopano, inu mukuona, Yesu ndi aneneri awa, chirichonse chimene iwo ankachikamba chinkayenera kukhala chiri choona, pakuti iyo inali mphamvu ya Mulungu mwa iwo, Mulungu Mwiniwake akuyankhula kupyolera mwa iwo za kudza Kwake komwe Kwayekha kwa Ulemerero Wake womwe.

67 "Purezidenti ndi ndani? Ndani ati akhale, ati akhale? Kodi ife tikhala ndi mvula yokwanira chaka chino?" Izo sizikutanthauza kanthu. Chinachake cha kwa ulemerero wa Mulungu, chinachake choti chiukhazikitse Mpingo mu dongosolo, chinachake kwa mphamvu ya Mulungu; osati kuti udzipangire wekha dzina, koma kuti upange ulemerero wa Mulungu kuwonetseredwa.

68 Tsopano ife tikuzindikira kuti aneneri onse awo ndi zonse zomwe iwo ankanena za Iye, chirichonse chinabwera moona chifukwa Iye anali chimake cha Chipangano Chakale. Yesu, Mesiya, Mesiya wakudza, anali chomwe mneneri aliyense ankayang'anako—kuchokera kwa Adamu mpaka Malaki. Mneneri aliyense ankayankhula za kudza kwa Ambuye. Aliyense ankaika gawo lake umo chifukwa iye anali wodzozedwa wa Mulungu. Ndi zonse iye akanakhoza kuziyankhula.

69 Tsopano, ndikukhumba ife tikanakhala ndi nthawi yochuluka pa izo. Koma, penyani, chirichonse chimene iwo ankanena chimafika pochitika. Taonani kuno, tiyeni tingotenga zina za zinthu zomwe aneneri ananena.

70 "Namwali adzaima ndipo adzabala mwana." Kodi izo zinachitika? Zedi. "Dzina Lake adzatchedwa Emanueli, Kalonga wa Mtendere, Mulungu Wamphamvu, Atate osatha." Ndi chimene Iye anali, ndendende, "Atate wosatha." Palibe munthu ati azitchedwa "Atate," pa dziko lapansi pano, koma Mulungu ndiye Atate wanu.

71 Chabwino, tsopano tiyeni tiwone kachiwiri. "Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, iye anatunduzidwa chifukwa cha kusaweruzika kwathu; chilango cha mtendere wathu pa iye, ndi mikwingwirima yake ife tinachiritsidwa." Nyumba ya chiweruzo ya Pilato, pamene munthu yemwe, ali ndi nsana wochekedwa monga choncho ndi kucheka kwa chikwapu cha michira-naini, sankazindikira kuti Malemba ananena kuti izo zikanadzakhala mwanjira iyo. Iwo analibe kuzindikira kwa mzimu, ansembe aja omwe anati "Kutali ndi Iye, kutali ndi Iye."

72 Ndipo pa mtanda pamene iwo ankamupotozera milomo yawo, ndi zinthu monga choncho, pamene iwo anamumva Iye akulira. "Mulungu wanga, nchifukwa chiani Inu mwandisiya Ine?" Iwo analibe kuuzindikira. Mwaona, iwo sankakhoza kuuzindikira Mzimu. Ndi chimene Davide anali kuchikamba mu Salmo ya 22, iwo ankapotoza milomo yao mosadziwa kuti iwo anali kuchita izo. Chimodzimodzi basi monga wachi Benjamini uja anachitira kwa Davide. Mwaona, iye ankaganiza Davide anali yense wolakwitsa chifukwa iye sankagwirizana ndi iye pa mfundo zake za kuyendetsa ufumu wake. Iye sanali kumvetsa izo kuti uwo unali Mzimu wa Mulungu mwa Davide ukuchita izo.

73 Ndi kumene ife tiyenera kumazindikira, lero, mzimu wa munthu. Kodi iye akuyesera kuchita chiani? Kodi iye akulinga chiani? Osati gulu lomwe iye alimo, kapena chomwe ichi, icho, kapena chimzake, kaya iye ndi munthu woyera, munthu wakuda, munthu wachikasu, kapena chirichonse iye ali. Tiyeni tiwone chimene iye akuyesera kuti apindule, ndi kuchitenga icho, tiwone chimene iye akuyesera kuti achite kwa Ufumu wa Mulungu. Iye ali nawo malingaliro osamvetseka kwa athu, ndi zabwino mwangwiro ngati iye akuyesera kuti akwaniritse chinachake kwa Ufumu wa Mulungu. Zizindikireni izo mwa iye. Ngati iye akulakwitsa, ndi woona mu mtima, Mulungu adzamubweretsa iye mpaka ku Choonadi cha chinthucho pakapita kanthawi. Msiyeni iye yekha, msiyeni iye yekha, muone chimene iye akuyesera kuti achite.

74 Tsopano ife tikuona pano, ndiye ife tikuzipeza mu Yake—mu imfa Yake, pamene Iye anafa pa mtanda, ndi kumalira zinthu zonse zomwe aneneri ankanena za Iye, "Iwo alasa manja Anga

ndi mapazi Anga." Apo izo zinakwaniritsidwa. Aneneri anali kulondola. Iwo ankaganiza kuti anali iwoeni kapena ankalira ngati kuti anali iwoeni, koma izo zinawonetseredwa mu mtanda.

75 "Iye—Iye anawerengedwa ndi olakwa." Ndi chimene iye anachitidwa. Iye anali ndi olakwa. "Mu imfa Yake Iye anapanga koikidwa Kwake ndi olemera." Iye anatero, Iye anaikidwa mu manda a munthu wolemera. "Ine sindidzausiya moyo Wake. . . Iye sadzausiya moyo wanga," anatero Davide, Mzimu wa Mulungu mwa Davide ukuyankhula momveka. "Iye sadzausiya moyo wanga mu hade, ngakhalenso Iye sadzalola Mmodzi woyera Wake kuti awone chivundi," ngati kuti Davide akanadzakhala Mmodzi woyerayo. Uyo sanali Davide, uwo unali Mzimu wa Mulungu mwa Davide ukufuulira. Mwaona, Mzimu wa Mulungu mwa munthu ukufuulira.

Ena a iwo anati, "Tamvetserani kwa wachinyengo uja kumtunda uko."

76 Iye sanali, iwo unali Mzimu wa Mulungu mwa iye ukufuulira. Mwaona, Mzimu wa Mulungu ukudziwonetsera wokha, "Osausiya moyo Wake mu hade, kapena kuti Iye alole Mmodzi woyera wanga kuti awone chivundi."

77 Tsopano, abwenzi, potseka, ndiroleni ine ndinene ichi, nthawi yathu ikutha. Koma, taonani, ndiroleni ine ndinene izi potseka, ndi Malemba awa pano. Tiyeni tiwone. Ngati munthu, kuti nkhani yonse ya Chipangano Chakale inali ya Iye, aneneri onse oyera odzozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, ngati zonse izo ndi chirichonse chimene iwo ankanena chinakwaniritsidwa mpaka lembo ndendende mwa Iye, zedi Munthu wamkulu uja wotchedwa Mwana wa Mulungu ayenera kuti azidziwa momwe angakhazikitsire Mpingo wa Chipangano Chatsopano. Kodi inu simukukhulupirira izo? Iye ayenera kukhala ndi lingaliro lodziwira momwe angaukhazikitsire Mpingo wa Chipangano Chatsopano.

78 Chinthu choyamba chimene ine ndikufuna kuitanira kwa tcheru chanu, cha kuno mu Mateyu, mutu wa 16, kuti pamene Iye—Iye akuyankhula ndiye, pamene Iye anabwera uko ndipo anali kuyankhula kwa ophunzira. Iye anati, "Kodi anthu akuti Ine Mwana wa munthu ndine yani?"

79 Ndipo iwo anati, "Ena akuti Ndinu 'Eliya,' ndipo ena akuti Ndinu 'Wakuti-n-wakuti,' ndipo ena akuti Ndinu 'Wakuti-n-wakuti,' ndi monga choncho, ena osiyana."

Iye anati, "Koma inu mukuti Ine ndine yani?"

80 Ndipo Petro anati, "Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo."

81 Iye anati, "Wodala ndiwe Simoni, mwana wa Yona, pakuti thupi ndi mwazi sizinaulule izi kwa iwe, koma Atate Anga omwe ali Kumwamba awululira izi kwa iwe. Ndi—ndipo ine

ndikuti kwa iwe kuti iwe ndi Simoni, kapena Petro, ndipo pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizingakhoze kuwulaka Iwo." Tsopano, apo ife tikuyankhula za Mpingo. Tsopano penyani mwatcheru, ndipo, ngati ine ndikulakwitsa, Mulungu andikhululukire ine ndipo inu mundikhululukire ine.

82 Tsopano, m—mpingo wa Katolika umanena kuti "Uwo unali mwala womwe unali pamenepo, Petro, ndipo pa Petro Iye anamangapo Mpingo." Tsopano, ife tikudziwa kuti uko ndi kulakwitsa. Ife Achiprotestanti timatsutsana ndi izo.

83 Koma ife Achiprotestanti timati, "Izo zinali *Iyemwini* pamene Iye anamangirapo Mpingo Wake, Iyemwini." Koma, ngati inu mungazindikire, ine ndikufuna kutsutsana ndi izo, mwaubwenzi. Si zinali izo.

84 Izo zinali pa *vumbulutso* lauzimu la Iyemwini. Mwaona? "Thupi ndi mwazi . . . " Iwe sunaphunzire konse izi mu seminare, monga izo ziri zabwino. Iwe sunaphunzire izi ndi chikhulupiriro china cha mpingo, monga icho chiri chabwino. Ndi chabwino, koma thupi ndi mwazi sizinaulule izi kwa iwe. Ilo si lingaliro laluntha la momwe iwe ungapangire mayankhulidwe ako, momwe iwe uyenera kudziweramitsa wekha, momwe kapena chinthu chachikulu chimene iwe uyenera kuchita kuno pa dziko lapansi. Izo si zomwe ziri. Izo si kumanga chinthu chachikulu kapena kuchita chinthu chachikulu. Chomwe chiri ndi vumbulutso la Mawu a Mulungu. Iye anali Mawu. "Pa chiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anapangidwa kuonekera ndipo anadzakhala pakati pathu." Iye anali . . . lija linali vumbulutso la Mawu a Mulungu.

85 Mzimu mwa Petro ukuulula mwa vumbulutso lauzimu kuti Iye anali Mwana wa Mulungu atapangidwa kuwonekera. Mulungu wa Ulemerero akuwonetsera ulemerero wa Mulungu. "Pa thanthwe ili (vumbulutso lauzimu la Mawu) ine ndidzamangapo Mpingo Wanga." Chifukwa? Ngati aneneri aja anali pansi pa Mulungu, akuyankhula mwa Mzimu Woyera kuti uyo anali Mwana wa Mulungu, Mzimu womwewo ku mbali iyi ukuulula mobwerezanso chinthu chomwecho. Kodi inu mukuziona izo?

86 "Thupi ndi mwazi," iwe sungakhoze kuziphunzira izo mu seminare. Inu mumakaphunzira zanu . . . mumakatenga D.D. yanu ndi Ph.D. yanu ndi L.D., kapena . . . Izo zonse ndi zabwino, ndikukhumba ine ndikanakhala nazo izo. Ndiko kulondola, komabe si Ndicho ayi. Inu simusowa kuti mukhale nazo izo, komabe nzabwino kukhala nazo. Inu mukhoza kukhala Ichi, nkuonjezera; koma ngati inu muti kufute zoonjezerazo, tengani Ichi. *Ichi* ndicho Icho. Ngati izi si Icho, ndiroleni ine ndikhale nacho Ichi mulimonse. Ine ndikuchifuna Ichi! Ichi!

87 "Thupi ndi mwazi sizinaululire izi kwa iwe." Iwe sunaphunzire konse izo kudzera mu mzere wa maphunziro. Iwe sunaziphunzire konse izo kudzera mu mzere wa chipembedzo. Izo ndi zabwino, maphunziro, chipembedzo ndi chabwino. Ndilo gawo la izo. Koma anthu akugonera mochuluka kwambiri kwa icho ndipo iwo akusiya kuzindikira kwauzimu. Mwaona?

88 "Thupi ndi mwazi sizinaululire izi kwa inu, koma Atate Anga omwe ali Kumwamba awululira izi kwa iwe. Ndipo pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizingakhoze kuwulaka Iwo." "Sizidzakhoza kuwulaka," zikusonyeza kuti iwo azidzautsutsa Iwo.

89 Tsopano penyani ndipo muwone pamene zipata za gehena ziri kutsutsa. Izo siziri kutsutsa zipembedzo. Boma limazidziwa izo. Izo siziri. Dziko limazizindikira zipembedzo zathu, zonse izo. Ife tiri nawo ufulu, aliyense wa ife ngati mbadwa za Chimereka, ife tiri nawo maufulu a chipembedzo, zomwe ziri zabwino, ife timayamikira izo. Koma sindizo zomwe zipata za gehena zikutsutsa. Izo zikutsutsana ndi vumbulutso lauzimu la Khristu kukhala pano tsopano, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndicho chimene izo zikutsutsa. "Zipata za gehena zizidzawatsutsa Iwo, koma izo sizidzaugonjetsa."

90 Ndi inu pamenepo, kuzindikira kwauzimu. Mosasamala yemwe iye ali, iye ndi m'bale wanga bola ngati iye akuyesera kuti akwaniritse cholinga chomwecho chimene ine ndikuchigwirira ntchito. Kaya iye ndi mneneri, kaya iye ndi m'busa, kaya iye ndi dikoni, kaya iye ndi wakuti-n-wakuti, kaya Mulungu amulemekeze iye mwanjira iyi, mwanjira *iyo*, chirichonse chomwe chiri, kusandilemekeza ine, chirichonse chomwe iye akufuna kuchita, komabe uyo ndi m'bale wanga. Ife tikugwirira ntchito chinthu chomwecho. Ife tikutumiza athu—athu . . . ntchito zathu zonse mu Ufumu womwewo kutaliko. Iye akugwirira ntchito chinthu chomwe ine ndiri. Kuzindikira kwauzimu, vumbulutso lauzimu la Mulungu. Penyani kuno, ngati inu mukufuna . . .

91 Yesu . . . Ine ndinalalikira usiku wina kwinakwake, mwina kumusi uko, "Izo Sizinali Chomwecho Kuyambira Pachiyambi." Ife tiyenera kubwerera ku chiyambi kuti tikaupeze mutu wathu tsopano kwa mphindi yokha. Pachiyambi uko kunali Kaini, waluntha, anamanga mpingo wabwino (ife tikanati), anapanga guwa labwino, anaperekapo nsembe, anapemphera, modzipereka, anapereka kuthokoza, anapereka chakhumi chake, chirichonse mwachipembedzo basi monga Abele anali.

92 Koma Abele, (uko kunalibe Baibulo mu masiku amenewo), koma mwa vumbulutso Lauzimu iye anaona kuti izo si zinali zipatso za mmunda zomwe zinatipangitsa ife kuchimwa, iwo sanali maapulo omwe iwo anawadya. Mukuona, iwo sanali maapulo, vumbulutso linamuuza iye izo. Ndipo si zinali zipatso

zomwe zinamupangitsa iye kuti atulukire pamenepo. Iwo unali moyo, kulekanitsa kwa moyo; chotero iye anapita ndipo anakatenga mwanawankhosa ndipo anamupereka iye mmalo mwake mwa chikhulupiriro, lomwe liri vumbulutso lauzimu. Ameni! Vumbulutso la Mulungu, vumbulutso lauzimu lomwe linaululidwira kwa iye. Si chipatso, si maapulo, si mapichesi, nthuza ndi mapeyala. Kunali kulekanitsa kwa moyo, chotero iye anapita ndipo anakautenga moyo ndipo anaupereka iwo mmalo mwa chipatso.

93 Zipatso ndi zomwe iwe umadya, ntchito zako ndizo manja ako omwe. Chimene iwe umachita apa, "Ine ndipita ndikamange *ichi*. Ine ndipita ndikamange *ichi*. Ine ndikathandizira *icho*." Izo nzabwino. Iye anali ndi guwa mofanana basi monga enawo analiri. Onse a iwo anali ndi maguwa. Izo zinali zabwino.

94 Koma chinali choonadi choululidwa mwauzimu cha chinthucho, pakuti Mzimu wa Mulungu unaulula izo, "Ndipo pa thanthwe limenelo, thanthwe lomwe Khristu anaferapo, Thanthwe la mibadwo, pa thanthwe pomwe mwanawankhosa wa Abele anaferapo." Abele wamng'ono uja pamene iye ankaika manja ake pa mwanawankhosa wamng'ono uja, ndi ubweya wake waung'ono woyera ukusambitsidwa pamene iye anatenga—mwala, iwo analibe chochekera mu tsiku limenelo, ndipo anagagada khosi lake laling'ono monga choncho ndi kulisasantha ilo. Ndipo kanthu kakang'ono kosauka kakufa, magazi akusambitsa manja ake, ndipo ubweya wake waung'ono wonse utasambitsidwa ndi magazi, kakuphiriphita ndi kulira.

95 Kodi izo zinkayankhula za chiani? Mwanawankhosa wa Mulungu, zaka foro handiredi zina mtsogolo, ataululidwa mwauzimu mpingo ukumukana Iye. Ndipo anthu anamutcha Iye "Belezebule" ndi "mdierekezi," chifukwa aneneri onse anali atayankhulapo. Iwo anawakana aneneri. O, Iye anati, "Inu mumamanga manda awo, ndipo ndinu munawaika iwo mmenemo. Inu mumakongoletsa makoma," Iye anatero kwa iwo. Popanda kuzindikira kwauzimu, asakudziwa kuti uyo anali Mwanawankhosa wa Mulungu. Kuti iye ankayenera kuti akhale mwanjira imeneyo ndi kuchita mwanjira imeneyo, chifukwa iye anali kukwaniritsa Mawu a Mulungu.

96 Ndipo Mpingo wa Mzimu Woyera lero, ukuchita momwe iwo akuchitira, kumachita zinthu zomwezo iwo akuchita, iwo akukwaniritsa Mawu a Mulungu. Aleluya! Mwaona, Petro anati, pa tsiku la Pentekoste, "Ichi ndi chija." Ndipo iye anati, "Iwo uli kwa inu ndi kwa ana anu, ndi iwo omwe ali kutali, ngakhale ochuluka amene Ambuye Mulungu wathu ati adzawaitane."

97 Aneneri odzozedwa omwe aja anati Kuwala kwamadzulo kukanadzawala, pakanati padzakhale mvula yanyundo ndi yamasika palimodzi monga mu masiku a chisomo. Onani apa. Ndi chiani icho? Mvula yanyundo ikubwerapo, ndipo

mvula yamasika yadutsa nthawi yake. Ndiye izo zalumikizana, ndipo ziri palimodzi, mvula yanyundo ndi yamasika palimodzi, Mzimu Woyera kukhala utawonetseredwa mwa mphamvu ndi chiukitsiro cha Yesu Khristu. Ndi zimenezotu, zikubwera palimodzi, yanyundo . . . chisomo cha Mulungu! Iye anati, "Monga zinali mu masiku a Nowa." Chisomo chake chinali chopirira motalika. Pano izo ziri lero, kupirira motalika, kulumikizana. Akubweretsa mtambo wa ku masiku akale ndi mtambo wa tsiku lino, palimodzi. Mvula yanyundo inathamangiramo poyamba, mvula yoyamba ife tinali nayo, tsopano pano pakudza mvula yamasika ikubwerapo, mvula yanyundo ikubwera pamwamba pa mvula yamasika, kummawa ndi kumadzulo kukomana palimodzi. Mvula zonsezo kumagwera limodzi, machiritso Auzimu kuonjeza Mngelo wa Mulungu akuulula zinsinsi za mitima ndi kumabweretsa chirichonse pochitika. O, zimawoneka ngati mwana wobadwa moona wa Mulungu akanachiona icho. Ndi zimenezotu, Mzimu ukuulula vumbulutso. Ndicho chimene Yesu anati Mpingo ukanati udzamangidwirepo.

98 Chabwino, ndiye wina akhoza kuukapo ndi kuti, "Chabwino, zedi, ife Akuti-ndi-akuti, ife tinamangidwa pa Ilo."

99 Tiyeni titenge Mawu Ake mopitirira pang'ono. Kutuma kotsiriza kwa Mpingo Wake, Iye anati, "Pitani inu ku dziko lonse ndi kukalalikira Uthenga kwa cholengedwa chirichonse." Dziko lonse. Kodi izo zikathera kutali bwanji? Dziko lonse. Kwa angati? Cholengedwa chirichonse. "Iye amene akhulupirira ndipo akabatizidwa," osati mpingo, "iye" ndi puronauni yaumwini. "Iye amene akhulupirira," wapayekha.

100 Monga David DuPlessis ananena za zidzukulu, mulibe zidzukulu mu Ufumu wa Mulungu, ndi ana! Bambo anu anali Achipentekoste ndipo inu mukungobwera kuno ku mpingo uno chifukwa iwo amabwera kuno ku—ku Eleventh ndi Garfield, analandira Mzimu Woyera, amangokubweretsanimo inu ngati chidzukulu, inu mukulakwa! Mulungu ayenera kuti adziululire Yekha kwa inu.

101 Ndipo palibe munthu yemwe angakhoze kumutcha Yesu Khristu mwa lingaliro laluntha. Palibe munthu angakhoze kumutcha Yesu kuti ndi Khristu chifukwa iye akumva chisoni ndi machimo ake ndipo akubwera kudzalapa. Palibe munthu angakhoze kumutcha Yesu kuti ndi Khristu, kokha mwa . . . vumbulutso ilo la Mzimu Woyera kupangitsa izo kudziwika kwa iye. "Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzaugonjetsa konse Iwo." Ndi limenelo vumbulutso. Ndi ilo apo, pamene Iye wamangapo Mpingo Wake.

102 Ndani anachita izo, Petro? Ayi, ayi, ayi. Ndani anachita izo? Khristu anati, "Vumbulutso la Mulungu, Mzimu Woyera ukanati ulibweretse ilo kwa inu. Kanthawi pang'ono ndipo

Ine ndikusiyani inu, koma Ine ndipemphera Atate ndipo Iye akutumizirani inu Mtonthozi, adzabweretsa zinthu izi ku kukumbukira kwanu." Ndi kulondola uko? Kodi Iye akuchita chiani mmawa uno. Ndipo adzachita chiani? "Adzakusonyezani inu zinthu zakudza." Mzimu Woyera mu Mpingo mu masiku otsiriza.

Tsopano inu mukuti, "M'bale, aleluya, ndiwo mpingo wanga."

103 Dikirani miniti! Yesu anati, "Ichi anthu onse adzadziwira kuti ndinu ophunzira Anga," mu Yohane Woyera 13:35, "Ichi anthu onse adzadziwira kuti ndinu ophunzira anga, pamene inu muli nacho chikondi wina kwa mzake." Choonadi choululidwa ndi Mzimu cha Ufumu wa Mulungu uli nkudza, kuyang'ana kunja ku mapeto kutaliko, kumawona chimene aneneri ankachilirira, kumaona chimene Yesu ankachiyankhula, ndipo pano Mzimu Woyera womwewo mwa inu ukulirira mmbuyo momwe, "Uko nkulondola! Uko nkulondola!" Ndi chiani icho? Ndi Choonadi choululidwa mwauzimu. Ine ndikumukonda m'bale wanga mosasamala kumene iwo amapita mwa mpingo, kaya iwo ndi ayanyundo kapena yamasika, kapena opanda mvula nkomwe, bola ngati iwo ali mu Thupi la Khristu, akuyesera kuti apindule. Osati chinachake kwa cholinga chinachake ku—kuti mudziwonetsere nokha pa dziko lapansi, koma cholinga cha Ufumu wa Mulungu ndi ulemerero wa Kudza Kwake, kuti awulule ndi kupangitsa kudziwika Kuwonekera Kwake kwaposachedwa.

104 Tsopano, potseka, ife tikufuna kuti tiganize za ichi. "Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga," kukhoza. Ndiyeno ife tikupeza, uko mu Yohane 14:7, Iye ananena izi, "Ntchito zimene Ine ndikuzichita, inu muzidzazichita nanunso. Ntchito zimene ine ndikuzichita." Kodi Iye ankachita ntchito za mtundu wanji kuti adzipangitse Yekha kudziwika? Inu mukukumbukira za Petro, sichoncho inu? Zomwe ife takhala tikuzikamba, za Filipo, mkazi pa chitsime. Kuneneratu izo kuti zisapite kwa Amitundu, koma zikanadzakhala ziri mu masiku otsiriza, monga Iye anati, "Monga izo zinali mu masiku a Sodomu, chomwecho izo zidzakhala ziri mu kudza kwa Mwana wa munthu." Apo pali vumbulutso litalembedwa mu zinsinsi monga izi, kwa dziko lakunja, kwa dziko lomwe silimadziwa kanthu za Iwo. Koma inu abale ofunika, inu alongo ofunika, inu sindinu ana a mdima, inu sindinu ana ausiku, koma ndinu ana a Kuwala, mukuyenda mu Kuwala monga Iye ali mu Kuwala, ndiye ife tiri nacho chiyanjano wina ndi mzake, pamene Magazi a Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, akutsuka machimo athu onse kwa ife tonse. Ndi inu apo, antchito a Ambuye.

105 Yesu . . . Pamene ine ndikubwereza Lemba langa cha apa, ine ndiri naye Marko 16, inde, Marko 16, Iye anati, "Pitani inu mu dziko lonse." Ndi uwu mtundu wa Mpingo

womwe Iye anaukhazikitsa. Kutumidwa kotsiriza kwa Mpingo, "Pitani inu mu dziko lonse, kalalikireni Uthenga kwa cholengedwa chirichonse. Iye amene akhulupirira ndipo akabatizidwa adzapulumutsidwa. Iye amene sakhulupirira adzalangidwa." Tsopano tayang'anani apa, tayang'anani pa kuzindikira kwauzimu uku... "Iye amene akhulupirira ndipo akabatizidwa." Iye sananene ndendende njira yake, koma ife timafuna tizikangana pa izo, mwaona, chinthu china. Mwaona, "Iye amene akhulupirira ndipo akabatizidwa adzapulumutsidwa." Mulimonse momwe iye akufuna kuti abatizidwire, izo ziri ndi iye. Ngati zopindula zake ziri za ku Ufumu wa Mulungu, tiyeni, m'bale. Ife tikuguba chamtsogolo ndi Mzimu womwewo. Ngati ine ndikulakwitsa, ndiye inu mudziwa, izo zidzachitika mwanjira iyo. Ndipo ngati inu mukulakwitsa, izo zidzakhala icho. Koma mitima yathu ndi zolinga zathu ndi zokhumba zathu ndi za kwa Ufumu wa Mulungu kutaliko. Kutaliko ife tiri, ife taloza ku Gologota.

106 Ine ndi malingaliro anga, chifukwa, ine ndiri...ine ndiribe m'bale yemwe amakonda mkate wa nthuza mwabwino monga ine ndimachitira, koma ndife abale. Mwaona? Palibe wa iwo amakonda kusaka ndi kuwedza monga ine ndimachitira, koma ndife abale. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Ine ndiri nawo malingaliro anga anga, koma izo sizimamupanga iye kusakhala m'bale wanga, bambo ake ndi bambo anga, banja lake ndi banja langa. Ndi inu apo.

107 Mbadwa zonse zinkasiyana wina ndi mzake, koma apo panali bambo mmodzi ndipo izo ziyenera kugwirira ntchito kwa chinthu chimodzi, ndipo iwo anamukana mmodzi wamkuluyo mmenemo chifukwa iye anali wauzimu. Kodi inu simukuziona Izo, abale? Kodi inu simukukhoza kuwona zomwe ine ndikuzikamba?

108 Tsopano zindikirani, ndipo tiri...potseka, "Pitani inu mu dziko lonse, kalalikireni Uthenga kwa cholengedwa chirichonse. Iye amene ati akhulupirira ndipo akabatizidwa adzapulumutsidwa. Iye..." [Malo osajambulidwa pa tape—Mkonzi.] "Ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira; mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda, iwo azidzayankhula ndi malirime atsopano." Ndi chiani icho? Vumbulutso lauzimu. Mwaona? "Iwo azidzayankhula ndi malirime atsopano. Ngati iwo atola njoka kapena kumwa zinthu zakupha, izo sizidzawapweteka iwo. Ngati iwo adzaika manja awo pa odwala, iwo adzachira." Izo zinali chomwe Mpingo Watsopano unali. Ndiwo mtundu wa Mpingo umene Yesu Khristu, Mmodzi wamkulu uyu yemwe aneneri onse anafuulira kuti akanadzachita. Ife tikuupeza Mzimu Wake ukubwera cha kuno ndipo akuneneratu kuti Mzimu Wake mwa anthu ukanadzabwerera kumene ndi kudzachita zinthu zomwe Iye ankazichita.

109 Nditatseka ine pa kunena izi. Ine ndiri nawo pafupi Malemba ena dazeni pano, koma ife tiribe nthawi. Mwaona? Koma mvetserani kwa izi. Nditatseka ine pa kunena izi. Mneneri aliyense woona wobadwa-kachiwiri wa Ambuye, mlaliki, mphunzitsi wa Sande sukulu, mpenyi, mtumwi, mmishonare, chirichonse chomwe iye angakhale ali, mtima wake wonse wakhazikika, ndipo iye ali wodzazidwa kwambri ndi wodzozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, wodzozedwa kwambiri. Chirichonse chomwe udindo wake uli, chirichonse chomwe iwo ungakhale, kuti azilalikira, kapena kuti aziphunzitsa, kapena kuti azifalitsa uthenga, kapena kuti aziona masomphenya, chirichonse chomwe chiri, iye azichita izo kwa Ufumu wa Mulungu. Ndipo Mzimu wa Mulungu uziyankhula mobwereza kudzera mwa munthu yemweyo ndi kumawonetsera kuti ndi Ufumu wa Mulungu.

110 Ndiye ife. . . Ine monga wa Baptisti, ine ndikakuonani inu Achipentekoste, ndinu m'bale wanga. Inu sindinu a mpingo wa Baptisti, ine ndiri. Ndi mpingo wokha ine ndinayamba ndakhalamo, unali mpingo wa Baptisti. Koma izo sizimayima mu njira yanga, ine ndimawona Mzimu wa Mulungu umene uli ndi inu. Ine ndimawona zomwe inu mukuyesera kuti muchite. Chabwino, ngati ine, Wabaptisti, ndingakhoze kumverera motero, zedi a Assemblies, a Mpingo wa Mulungu, a United Pentekoste, a Independents, ndi ife tonse abale limodzi tiyenera kumawona kuti tikuyesera kuti tigwirire ntchito kwa cholinga chimodzi. Tiyeni tikhale ndi kuzindikira kwauzimu.

111 Tsopano mvetserani. Pakutseka, ine ndipanga ndemanga yotsiriza iyi. Ambiri ali odwala ndi ofooka pakati pa inu, ndipo ambiri akugona, akufa mwauzimu, chifukwa iwo alibe kuzindikira kwa Thupi la Khristu. Thupi lodwala ili lomwe ife tiri nalo! Mulungu atithandize ife kuti tikhale ndi kuzindikira kwauzimu kwa vumbulutso ilo la Ufumu wa Mulungu ndi la chikondi cha Mulungu mu mitima yathu, chokhetsedwa mmenemo ndi Mzimu Woyera, kuti tiziyesera kuyika mikono yathu kunja, nkuti, "Ife ndi abale." Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Ndipo mphatso yaing'ono iliyonse yomwe inu muli nayo, musati muzigwiritsa iyo ntchito poyesera kuti mupange chinachake chachikulu kwa ifeeni, tiyeni tizipangire izo kwa Ufumu wa Mulungu, kuti tizigwira ntchito ndi aliyense, kuti tiyesere kukweza cholinga cha Yesu Khristu, pakuti Kudza Kwake kuli posachedwapa. Kodi inu mukukhulupirira izo?

112 Ine ndikupepesa kwambiri kuti ndakusungani inu motalika kwambiri. M'bale David adzakhala kuno mawa kuti adzakuphunzitseni inu Malemba, koma pakali pano tiyeni ife tiweramitse mitu kamphindi kokha. [M'bale ayankhula mu lirime lina. Mlongo apereka kutanthauzira—Mkonzi.]

Tiyeni, asilikari Achikhristu!
Kuguba waku nkhondo,

Ndi mtanda wa Yesu
Uli patsogolo;
Sindife ogawanika,
Tiri thupi limodzi;
Chiyembekezo chimodzi ndi chiphunzitso,
Amodzi mu chikondi.

Tiyeni, asilikari Achikhristu! (inu mukukhulupirira inu muli? Kwezani dzanja lanu)
Kuguba waku nkhondo, (ndi chiani?)
Ndi . . . (cholinga chathu) Yesu
Ukupita patsogolo.

Mulungu akudalitseni inu. Abusa anu.

Kuuzindikira Mzimu CHA60-0308
(Discernment Of Spirit)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingelezi pa Lachiwiri mmawa, Marichi 8, 1960, ku First Assembly Of God mu Phoenix, Arizona, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 2002 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2002 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

Voice Of God Recordings, Malawi Office
P.O. Box 51453, Limbe, Malawi

Voice Of God Recordings
P.O. Box 950, Jeffersonville, Indiana 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org